# BWAILA CLUSTER TERM ONE EXAMINATIONS

## 2022-2023 JUNIOR CERTIFICATE OF EDUCATION

# CHICHEWA

**Subject Number: J032/I**

**Wednesday, 7th December 2022** **Time Allowed: 1hr 30 min**

**11:00AM – 12:30PM**

## PEPALA LOYAMBA

**(Malikisi 50)**

**Malangizo**

1. **Onesetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi limodzi.**
2. Pepala ili lili ndi magawo atatu **(A, B, ndi C).** Yankhani **mafunso onse** m'mgawo **A**. M'gawo **B**, yankhani funso limodzi ndipo yankhani mafunso onse m'gawo **C**.
3. Lembani **dzina lanu** pamwamba pa masamba **onse**.
4. Muchitebulo chili pamwambachi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lili kutsogolo kwake
5. Perekani pepala kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1-20 | | | |
| 21 | | | |
| 22 | | | |
| 23 | | | |
| | | | |

© 2022 BWAILA CLUSTER **Onani paseri/…**

# GAWO A: (Malikisi 20)

**Langizo:** Zungulizani lembo lokhoza (**A**, **B**, **C** kapena **D**) m'mafunso otsatirawa

**Mafunso 1 mpaka 4: Sankhani mitundu ya alowammalo yemwe watsekedwa mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi.**

**1.** Tanga tili ndi nzeru.
- A. Wamgwirizano
- B. Waumwini
- C. Wochulutsa
- D. woloza

**2.** Amene wadya mango timudziwa.
- A. wotsimikiza
- B. wamgwirizano
- C. waumwini
- D. wofunsa

**3.** Wayani akuvutitsa mwana wa ine?
- A. Woloza
- B. Wozichitira
- C. Wofunsa
- D. Wamgwirizano

**4.** Ndadya awiri okha.
- A. Wowerengera
- B. Waumwini
- C. Woloza
- D. Wamgwirizano

**Mafunso 5 mpaka 7:** Sankhani **magulu a mayina** olondola a mawu omwe adulidwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**5.** Mwana uja wabweretsa buku.
- A. Chi-, Zi-
- B. Li-, Ma-
- C. Mu-, A-
- D. I-, Zi-

**6.** Zidyo wagula chola kumsika.
- A. Mu-, Mi-
- B. I-, Zi-
- C. Chi-, Zi-
- D. Li-, Ma-

**7.** Wadya kanthutumba komwe ndinasunga.
- A. Ka-, Ti-
- B. Li-, Ma-
- C. I-, Zi-
- D. Chi-, Zi-

**Mafunso 8 mpaka 9:** Sankhani **kuchuluka kwa maphatikizo** a mawu omwe ali mmunsiwa.

**8.** Nkhwere
- A. Mawu aphatikizo limodzi
- B. Mawu amaphatikizo anayi
- C. Mawu amaphatikizo awiri
- D. Mawu amaphatikizo asanu ndi awiri

**9.** Chipsolopsolo
- A. Mawu amaphatikizo asanu
- B. Mawu amaphatikizo anayi
- C. Mawu amaphatikizo khumi ndi atatu
- D. Mawu amaphatikizo atatu

Mafunso **10** mpaka **13.** Tchulani **mtundu wa masinde** omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**10.** Mwana yemwe wabadwa dzulo kuchipatala ndi wamkazi.
A. Tsinde laubale
B. Tsinde la mlowammalo
C. Tsinde la dzina
D. Tsinde la mneni

**11.** Dalitso wagwira mbuzi zathu.
A. Tsinde loloza
B. Tsinde la mlowam'malo
C. Tsinde la mfotokozi
D. Tsinde la umwini

**12.** Musagule chimanga chachiwisi koma choumacho.
A. Tsinde la maonekedwe
B. Tsinde la muonjezi
C. Tsinde la malo
D. Tsinde loloza

**13.** Mabweredwe osapereka chilimbikitso atheretu.
A. Tsinde la dzina
B. Tsinde la mneni
C. Tsinde la muonjezi
D. Tsinde lochenjeza

**Mafunso 14 mpaka 16:** Sankhani **ntchito ya mphatikiri** yemwe watsekedwa mzere kumsi kwake m'ziganizo zotsatirazi.

**14.** Samalani wakawapatsa nsima agogo.
A. Kusonyeza mchitidwantchito
B. Kusonyeza nthawi
C. Kusonyeza mchitantchito
D. Kusonyeza kutsutsa

**15.** Abambo sanandigulire cholembera.
A. Kusonyeza kuti ntchito ikupitirira
B. Kusonyeza kuchuluka
C. Kusonyeza nthawi
D. Kusonyeza kutsutsa

**16.** Nanunso mukagwira chibalo mawa mukapita kusukulu.
A. Kusonyeza kuchuluka
B. Kusonyeza kubwereza kwa chinthu
C. Kusonyeza kutsimikiza
D. Kusonyeza nthawi.

**Mafunso 17 mpaka 20:** Sankhani matanthauzo oyenera a **zining'a, komanso mikuluwiko** yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi

**17.** Naliyera wawonda kwambiri chifukwa masiku ano walowa chamwaka
A. Akukhalira kudwaladwala
B. Wabereka mwana wakufa
C. Wakwatiwa ndi wakuba
D. Walowa chokolo

**18.** Mtsikana wosakana amuna uja wamwalira ataponda njati.
A. Atadwala matenda aakulu
B. Atatenga matenda pochita chiwerewere
C. Atakankhidwa ndi njati
D. Atanyozeka kwambiri

**19.** Anthu <u>adatsinira mafulufute kuuna</u> chifukwa chokuwiza akuluakulu aku boma.

A. Adatsekereza zabwino

B. Adapalamula

C. Adachita bwino

D. Adakwiyitsa alendo

**20.** Chifuniro <u>watchola bano</u> dzulo.

A. Wapalamula

B. watenga mimba

C. Watha msinkhu

D. watchola mango.

**Gawo B: (Malikisi 20)**

**Malangizo**

a. Yankhani funso **limodzi** lokha.

b. Lembani **chimangirizo** kapena **kalata.** Mawu a chimangirizo asachepere **150** koma asapitirire **200**. Malikisi adzaperekedwa, pakayalidwe ka chimangirizo, kapena kalata, malamulo a chiyankhulo, mfundo ndi kagwiritsidwe ntchito koyenera ka nsinjiro za chiyankhulo.

**21.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu:

‘Momwe tingachepetsere njala m’dziko’

**(Malikisi 20)**

**KAPENA**

**22.** Lembani kalata kwa Mkozi wa nyuzipepala ya Samala, P. O. Box 31100, Dekhani yomufotokozera za nkhanza zomwe ana a m’dera lanu akuchitiridwa.

**(Malikisi 20)**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

**Gawo C. (Malikisi 10)**

**Langizo:** Yankhani mafunso onse m'gawo ili

**23.** a. "Ndinafotokoza kuti sikoyenera aliyense aziyendayenda kunja pomwe amnzake akuphunzira. Poti

simunafune kumvera, lero mwaponda muufa"

i. Kodi malonjewa akuchitikira kuti?

________________________________________________ (Malikisi 1)

ii. Mawu oti,"mwaponda muufa" akutanthauzanji?

________________________________________________ (Malikisi 2)

iii. Ndi zilango **ziwiri** ziti zomwe wochita khalidweli angapatsidwe?

________________________________________________ (Malikisi 2)

b. Lembani malangizo **awiri** omwe mungapereke kwa mnzanu wokhudza ubwino wokhala ndi ufulu wachibadwidwe ndi udindo pasukulu.

i. ________________________________________________ (Malikisi 1)

ii. ________________________________________________ (Malikisi 1)

c. Tchulani njira **zitatu** zomwe mungafalitsire mauthenga a njira zamakono zaulimi.

i. ________________________________________________ (Malikisi 1)

ii. ________________________________________________ (Malikisi 1)

iii. ________________________________________________ (Malikisi 1)

**MAFUNSO ATHERA PANO**

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikidwa asanu ndi limodzi**